**PRESS RELEASE**

**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO**

**NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO**

# ULOSI WA NYENGO YA DZINJA WA CHAKA CHA 2025/2026

**MWACHINDUNJI: Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 ikuyembekezereka kukhala ndi mvula yamlingo okhazikika kapena kuposera apo. Kagwedwe ka mvulayi kakhala kosakhazikika kotero ndipofunika kukonzekera bwino.**

## Mau oyamba

Nyengo ya dzinja ku Malawi kuno imayamba mu October kufikira m'mwezi wa April. Nthambi yoona za nyengo ndi kusintha kwa nyengo ndiyomwe ili ndi ntchito yopanga kalondolondo/kauniuni wa zinthu zomwe zimabweretsa mvula m'dziko muno. Nyengo ya dzinja imakhazikika m'mwezi wa November kuyambira kumwera kwadziko lino ndipo pang'ono ndi pang'ono imafalikira m'zigawo zapakati komanso kumpoto. Mvula ya *Chizimalupsya* ndiyomwe imayambilira kugwa nyengo yadzinja isanakhazikike.

## Zomwe zimabweretsa mvula ku Malawi

Zinthu zikuluzikulu zomwe zimabweretsa mvula ndi monga nkumano wa mphepo zakum'mwera ndi zakumpoto kwa Africa, mpweya ochokera m'dera la Congo, m'pweya osakhazikika ochokera kumvuma, nkumano wa mphepo zozizira ndi zofunda kuchokera m'dera limodzi monga kum'mwera kokhakokha kapena kum'poto kwa Africa, kulemela ka m'pweya, mphepo za m'mwamba osaiwalanso katenthedwe ka madzi a m'nyanja zikuluzikulu monga za Pacific, India komanso Atlantic.

## ULOSI WA EL NINO KAPENA LA NINA

Njira zolosera nyengo padziko lonse zikuonetsa kuti gawo lalikulu la dzinja la 2025/2026 silikhudzidwa kwambiri ndi katenthedwe (*El Niño*) kapena kazizilidwe (La Niña) ka madzi cha kum'mawa kwa nyanja ya mchere ya Pacific, kutanthauza kuti mlingo wake ndi wa pakatikati. Komabe pali kuthekera koti miyezi ina yochepa idzakhudzidwa ndi La Niña. Zaka zodziwika zimene mbiri yake ikhoza kuyerekezedwa ndi dzinja la 2025/2026 ndizo; 1996/1997, 2013/2014, 2016/2017 ndi 2024/2025.

## Ulosi wa nyengo ya m'dzinja la 2025/2026 mwachidule.

Mwachidule ulosiwu uli motere:

a) **Kagwedwe ka mvula.**

- **October mpaka December 2025.** Madera ambiri mdziko muno akuyembekezereka kulandira mvula yamlingo okhazikika kapena kuposera apo, ngakhale madera ena a chigawo chaku mpoto akuyembekezereka kulandira mvula ya mulingo okhadzikika kapena kuchepera apo (map A). Pali chiyembekezo choti mwezi wa November madera ambiri adzakhala ndi mvula ya mlingo okhazikika kapena kuchepera apo.

- **January mpaka March 2026.** Tiyembekezere mvula yamlingo okhazikika kapena kuposera apo madera ambiri ngakhale madera ena am'maboma awa; Mchinji, Dowa, Kasungu ndi Lilongwe

akhoza kulandila mvula ya mlingo okhadzikika kapena kuchepera apo (map B). Pali chiopsezo choti dziko lonse la Malawi mu mwezi wa February kudzakhala mvula ya mlingo okhadzikika kapena kuchepera apo.

**b) Kuyamba kwa nyengo ya dzinja.**

Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kuyamba mochedwerako ndi masabata awiri m'madera ambiri. Izi zikutanthauza kuti nyengoyi idzayamba m'masiku apakati pa mwezi wa December. Koma madera ena am'chigawo cha kumwera monga; Blantyre, Thyolo, Zomba, Mulanje ndi Chiradzulu, nyengo yadzinja ikuyembekezereka kudzayamba mu nthawi yake, pakati pa mwezi wa November. Madera ena a boma la Mchinji nyengo yadzinja ikuyembekezereka kudzayamba m'masiku apakati kapena kumathero a mwezi wa November. Pali nkhawa yoti chiyambi cha nyengo ya dzinja chikhoza kukhala chosakhazikika.

**c) Mathero a nyengo ya dzinja**

Madera ambiri a dziko lino ayembekezere kuti nyengo yadzinja idzatha mu nthawi yake kapena mochedwerako imene ili kumathero a mwezi wa March kufikira kumayambiliro a mwezi wa April. Koma madera ambiri a m'chigawo chapakati ndi kumpoto nyengo yadzinja ikuyembekezereka kufika kumapeto m'masiku apakati pa mwezi wa April, ngakhale madera ena ochepa nyengoyi idzatha kumapeto a mwezi wa April.

**d) Kutalika kwa nyengo ya dzinja**

Nyengo ya dzinja ya 2025/2026 ikuyembekezereka kukhala yamasiku pafupifupi 130 kufikira 140 m'madera ambiri. Mlingowu ndi wa m'mene umayenera kukhalira, komabe madera ena am'maboma apakati ndi kumpoto akuyembekezereka kukhala ndi nyengo yadzinja yaifupi.

**e) Katenthedwe mu nyengo ya dzinja**

Tiyembekezere muyeso wakatenthedwe kudzakwera kwambiri kuposa mlingo okhazikika mu nyengo ya chilimwe maka miyezi ya December ndi February koma mu mwezi wa January pali chiyembekezo choti madera ambiri am'chigawo chapakati adzakhala ndi muyeso ozizilirako kuposa mlingo okhazikika. Katenthedwe aka kadzapereka chiopsezo chakutentha moonjeza (Heatwave).

**M'mene dzinjali lingatikhudzire**

Ngakhale dzinja la 2025/2026 likuyembekezeleka kukhala ndi mvula yochuluka, padzakhala kusiyana pakagwedwe ka mvula m'madera komanso kutalika kwa nthawi yogwera mvula. Mlingo wamvulayi ukuyembekezereka kuti ukhoza kukhala okwanira pa nkhani yaulimi, kuonjezera mlingo wa madzi mu nyanja zathu komanso madzi ogwiritsa ntchito zosiyanasiyana.

Kagwedwe ka mvulayi kakhoza kubweretsa ziopsezo monga; ng'amba maka mu mwezi wa February, njomba pakayambidwe ka dzinja, kutentha moonjeza zomwe zingapangitse kuti chinyezi chikhale chochepa mu nthaka komanso kubweretsa tizilombo ndi matenda ambeu. Mvula yamphanvu ikhoza kupangitsa madzi kusefukira komanso kukokoloka kwa nthaka zomwe zikupereka chiopsezo kumbeu komanso zomangamanga.

Nthambi zosiyanasiyana monga; a zaumoyo, zamadzi, zaulimi, zamaphunziro, mayendedwe, komanso zamphamvu akhoza kukumana ndi kusokonekera pakagwiridwe ka ntchito kamba ka madzi osefukira, anamondwe ndi kutentha moonjeza. Ulosiwu udzathandizira onse kukhala okonzeka ku ziopsezo zobwera ndi kusintha kwa nyengo ndi cholinga choteteza madera ndi chuma.

**Kagwiritsidwe ntchito ka ulosiwu**

Ulosi uwu ukufotokoza za dera lalikulu komaso nyengo yonse ya dzinja, ndipo sukufotokoza zonse zomwe zingamachitike mudela lochepa komaso mu kanthawi kochepa ngati pa tsiku kapena pa sabata. Pofuna kuti

zinthuzi zifotokozekedwe, Nthambi yowona zanyengo ndi kusintha kwa nyengo yatulutsa ulosi wa boma lililonse. Kuonjezera apo, ulosi wa tsiku ndi tsiku, wa masiku asanu, wa sabata, wa masiku khumi komanso zotsatira za zina zochitika mu nyengoyi ziziperekedwa mu nyengo yonse ya dzinjali. Nthambiyi iziperekanso mauthenga a ziopsezo ndi upangili wokhuzana ndi nyengo zovututirapo zomwe zingachitike mu nyengoyi.


Ogwiritsa ntchito ulosiwu monga a zaulimi, angozi zogwa mwadzidzidzi, oona za zamphamvu, ndi zamadzi akulimbikitsidwa kuti azifunsa upangili kuchokera kwa akatswiri akuunduna owona zimenezo pogwiritsa ntchito ulosiwu.

**Kuthekera kwa ulosi wa mvula: October mpaka December ndi January mpaka March**
Mmusimu muli mapu a ulosi wa nyengo ya dzinja ya 2025/2026 kuyambira October mpaka December ndi January mpaka march 2026 omwe waonetsa kuthekera kwa mlingo wa mvula.

**Mapu akumanzere (Map A)**, nyengo ya october mpaka December ikusonyeza kuti madera apakati komanso kumwera kwa dziko lino ali ndi kuthekera kolandira mvula ya mlingo okhazikika kapena kuposera apo. Koma pali kuthekera kolandira mvula yochepera mlingo okhadzikika madera a m'chigawo cha ku mpoto.

**Mapu akumanja (Map B)**, omwe ndi a nyengo ya miyezi ya January mpaka March, akusonyeza kuthekera kolandira mvula ya mlingo wokhazikika kapena kuposera apo. Koma madera ena amchigawo chapakati ali ndi kuthekera kolandira mvula yochepera mlingo okhadzikika.

**MAP A: OND 2025** | **MAP B: JFM 2026**




**Khalani odziwa, khalani okonzeka, khalani otetezeka mu nyengo ikubwerayi. Kutetezeka kwanu ndi kukhala wangwiro ndi chinthu chopambana kwa ife**

**Uthengawu wasindikizidwa pa: 12 September,2025**

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa: The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808, Blantyre, E-mail: metdept@metmalawi.gov.mw, Website: www.metmalawi.gov.mw***